UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NYENGO MSABATAYI

KUYAMBIRA PA 01 MPAKA PA 07 DECEMBER, 2025

NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyamba mawa lolemba pa 1 December 2025, tiyembekezere nyengo yofunda, yamitambo ndi yamphepo m'madera ambiri komanso ya mvula yamabingu yomwe nthawi zina idzigwa yamphamvu maka m'madera akumwera. Izi ndi kamba ka nkumano wa mphepo zochokera kumwera chakumvuma komanso zochokera kumvuma**. Mapu ali Kumanja akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula yomwe ikuyembekezereka m'sabata ikudzayi, kuphatikiza mvula ya sabata yonse. Mvula yochuluka ikuyembekereka kumwera ndipo izipita Ikuchepa tikamalowera chigawo cha pakati ndi kumpoto.**

M*phepo za Mwera zikuyembekezereka kuomba mwamphanvu pa nyanja zathu nthawi zina.*



Ulosi wamvula musabata ikudzayi. Kuphatikiza masiku onse musabatayi.

NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali nyengo ya mphepo, yamitambo ndi yotentha komanso mvula yamabingu yomwe m'madera ena inagwa yamphamvu**.** Ku Stella Maris ku Blantyre ndi komwe mvula inagwa yambiri ya mlingo wa **52.1mm** pa **28 November 2025.**

Mapu ali kumanja akuonetsa mlingo wa mvula yochuluka yomwe inagwa m'sabata yangothayi.

MALANGIZO M'SABATAYi

- **Pomwe mvula yamphamvu ikuyembekezereka m'madera ambiri akummwera,** tiyeni tikonze njira zonse zodutsa madzi pochotsa zinyalala kuti tipewe madzi osefukira.
- **Mvula yamabingu:** Tikhale m'malo otetezeka
- **Pa nyanja:** Asodzi akupemphedwa kupewa kulowa pa nyanja mphepo ya mphamvu ikamaomba.



Mapu akuonetsa kuchuluka kwa mlingo wa mvula m'sabata yangothayi

Kuti mudziwe zambiri funsani kwa: *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

Malo osindikizira: Blantyre **Yatulutsidwa Lamulungu pa 30 November, 2025**